Kudzoza kwa Madikoni

Ndipo, izo ziri, kuti choyamba ndi kuwakhazikitsa madikoni ena mu mpingo. Ndipo mpingo wathu waung'onowu pano ndi woyima pawokha. Iwo ulibe chipembedzo chirichonse kapena chirichonse choti chitumize madikoni ake, iwo umasankha madikoni ake ake. Iwo umasankha m'busa wake, iwo umasankha matrasti ake, iwo umasankha chirichonse chimene chimalowa ndi kutulukamo mu mpingo. Palibe munthu mmodzi ali nacho chonena pa chirichonse, ndi mpingo. Ndipo mpingo ndi iwo omwe amabwera ndi kumathandizira mpingo ndi kukhalapo kwawo, ndi chakhumi chawo ndi zopereka, ndiwo nthawizonse omwe amakhala nacho chonena chovomerezeka pa kukhazikitsa oterewa.

2 Ndipo ine ndikufuna kuti ndithokoze gulu la madikoni lathali, ndipo ine ndikuzinena izi kuchokera pano mmalo mwa mpingo wonse. Ngati aliyense wa abale awo ali pano, omwe anali M'bale Cox, M'bale Fleeman, ndi M'bale Higginbotham ndi M'bale Deatsman, iwo atipatsa ife kutumikira kwabwino, amupatsa Ambuye, mu Kachisi uyu.

3 Ndipo mwa kuwirikiza kulikonse, molingana ndi timalamulo ta mpingo, chaka chirichonse, madikoni kapena matrasti mosavutikira amakwaniritsa nthawi yawo. Ndipo ngati iwo akufuna kuti abwerere, chabwino. Ngati iwo sakufuna kuti abwerere, ndiye iwo akhoza kuyikamo ena mmalo mwawo, kuti gulu ili lapuma.

4 Ndipo usiku wina ine ndinaitana gulu la matrasiti, chomwe pali gulu latsopano la matrasti. Ndipo ine ndinamuwona M'bale Luther McDowell pano usikuuno, ndife okondwa kumuwona iye muno, yemwe anali mmbuyomo pa gulu la matrasti. Ine ndinapita uko sabata ino kuti ndikafufuze ndi kukapangitsa fotokope mapepala, omwe ati aperekedwe kwa mpingo, panonso. Kuti matrasti a mpingo tsopano ndi M'bale William Morgan, M'bale Mike Egan, ndi M'bale Banks Wood, ndi M'bale Roy Roberson. Ndipo onsewo ndi amu mzinda uno, kupatula M'bale Roberson yemwe amakhala pakati pa mizinda iwiri. Ambuye awona kuyenera mwa amuna amenewo, ndipo iwo akhala amuna olemekeza, ndipo iwo tsopano alandira udindo monga matrasti a mpingo uno.

5 Ndiyeno pamene msonkhano uwu unali kuchitika, ndipo zinanenedwa ndi m'busa wothandizira kuti ife . . . kusankha kwa gulu latsopano la madikoni, kuti awa atumikira nthawi yawo yatha n—ndipo apuma, ndipo zinali zoti pasankhidwe madikoni enanso. Tsopano, mpingo . . . Momwe izi zimachitidwira,

ndi, gululo likhoza kutchula madikoni, amuna omwe iwo ayanjana nawo ndipo awapeza kuti ndi olemekezeka ndi amuna olungama.

6 Udindo wa dikoni ndi udindo waukulu kwambiri, ndipo ndi waulemu waukulu kwa Ambuye kuti ukhale dikoni mu mpingo. Ndipo chotero, mu msonkhano usiku wina, mwamuna winawake anatchulidwira kwa ine. Ndipo pamene ndimakomana ndi m'busa, lotsatira . . . Lachisanu lapita ili, chimene chinali chovomerezedwa ndi mwamuna uyu kuti awa anali amuna olemekezeka ndi olungama.

7 Mnyamata mmodzi yemwe iwo anali atamupeza, sanali woyenera kwenikweni (si chifukwa kuti iye sanali mtundu woyenera wa mwamuna), uyo yemwe anatchulidwa ndi mmodzi wa amuna olemekezeka a gulu lathu la matrasti. Koma pamene abusa ndi ine tinabwera palimodzi, ndipo ine ndinafunsa usinkhu wa mnyamatayo, iye anali mu zaka zake za koyamba kwa makumi awiri. Wolemekezeka, wolungama, ndipo mwamuna weniweni, koma tinapeza kuti iye anali munthu wosakwatira. Baibulo limafuna dikoni kuti azikhala mwamuna wokwatira. Iye ayenera kuti azikhala mwamuna wa mkazi mmodzi.

8 Ndiyeno mwamuna wina yemwe anali mwamuna wolemekezeka kwambiri, woyenera kwambiri ku ntchitoyo ndipo akanakhala munthu wodzipereka, momwe m'bale anamutchulira iye. Ndiye pambuyo pa kufufuza nkhaniyo, nkuti m'baleyo wangobwera kumene mu Chikhulupiriro ichi, mkazi wake sakhulupirira mu Icho. Ndiye izo zamulepheretsa mwamunayo pa udindowo. Chifukwa iye ayenera kukhala nalo banja lake lonse likumumvera, iwo ayenera nawonso akhale mu Chikhulupiriro, chifukwa izo zingakhale zokanganitsa.

9 Ndipo ife tikumanga tsopano, ndipo ife tikukhumba kuti tiwukhazikitse mpingo uno. Ndipo monga woyang'anira zonse wa mpingowu, ine ndiyenera kumawona kuti izo zikusungidwa, Mwamalemba, chirichonse pa Mawu omwe.

10 Ndipo chotero apo, ndiye, izo zinapezeka zovomerezeka ndi gulu ili ndi m'busa, ndi woyang'anira zonse, kuti asankhiremo mu gulu ili la anthu pano amuna ena omwe ife tikuganiza kuti ndi amuna olemekezeka ndi olungama. Ife tikhoza kungowabweretsa iwo. Ndipo nzoti, kenako, iwo amasankhidwa ndi mpingo, ndi voti yawo. Ndiyeno amuna awa adzatumikira, ngati iwo ati amverere kuti awuvomereza udindo umenewu. Ndiye iwo abwera kwa nthawi yaifupi, kuti awone ngati iwo akumverera kuti mwina Mulungu wawaitana iwo. Ndipo ngati kenako, ngati iwo akumverera kuti iwo sali kuyenera, ndiye, iwo ali nawo ufulu mu masabata angapo otsatirawo kuti apume pa udindowo, kuti winawakenso akhoze kusankhidwira mu malo awo.

11 Komabe, pa chiyambi cha chitsitsimutso chomwe (ngati Mulungu alola) ine ndikufuna kuti ndikhale nacho kuno mu Kachisi uyu mwamsanga pamene ine nditi ndikhale nditapumapo, ndiye i—ndiye ine. . . ife tidzawadzoza madikoni amenewa pa kuwasanjika manja, madikoni ndi msungichuma mu mpingo uno. Koma choyamba iwo ayenera kuti asankhidwe n—ndi kuwona momwe iwo akuikondera iyo ndi momwe osonkhana akuzikondera izo. Ndiye ngati ziri—ndiye ngati ziri zololedwa ku mbali zonse, ndiye ife tiwapanga anthu awa kukhala madikoni odzozedwa, monga momwe Matrastii amasankhidwira mwanjira yomweyo.

12 Ndi kuyima kwapawokha ndi lamulo la mpingo, mwa Mawu a Mulungu. Chotero, kuti, iwo sangakhoze kungoti "Ine ndikuganiza bambo uyu angakhale bambo woyenera," izo siziri chomwecho, "M'bale Neville akuganiza kuti munthu uyu akanakhala bambo woyenera," kapena "gulu la matrastii likuganiza uyu angakhale bambo woyenera." Izo ziyenera kukhala mwa mpingo! Palibe wina yemwe amachita chirichonse mwa iyeyekha pano. Ndi voti ya mpingo. Ndi mpingo woyima pawokha.

13 Mpukutu wakale wa timalamulo unawonongeka mu kusefukira kwa 1937. Ife tazilembanso izo, ndipo zidzapachikidwa pa khoma kuno posachedwapa, ntchito za matrastii, madikoni, msungichuma, ndi ena otero, m'busa, wothandizira, ndi ena otero.

14 Mwa chisomo cha Mulungu, izo zanenedwa kwa ine, ndi voti ya zana pa zana kupyolera mu gulu lotumikira mpingo uno, kuti iwo apeza kuti M'bale Hollin Hickerson kuti ndi mwamuna wolungama, wolemekezeka, ndi wa mu mzere wa udindo uwu kuti alandire—ulemu waukulu wa kukhala dikoni wa pa Kachisi uno.

15 Ndiponso, ife tapeza, ndi mwa voti ya gulu lotumikira, kuti M'bale Collins nayenso wapezeka kuti ndi mwamuna wolemekezeka ndi wolungama. Pokhala mtumiki, iyemwini, kotero ife tikufuna kuti timufunse iye kuti abwere ndi kuti akhale d—dikoni wa mpingo; ndipo osati kokha dikoni, komanso wothandizira kwa M'bale Neville, ndi mwinamwake ku kalasi la Sande sukulu, kapena kuti azitenga malo a M'bale Neville, kapena chirichonse chimene chiri kuitanidwira pa iye kuti akhale wothandizira kwa M'bale Neville. Ameneyo ndi M'bale Collins.

16 Ndipo, panonso, mpingo wapeza, mwa kukonda, kuti M'bale Tony Zable, mwamuna wolemekezeka ndi wolungama, ndipo iye wakondedwa pamaso pa gulu la matrastii ndi abusa, kuti amufunse iye kuti alandire udindo wa dikoni mu Kachisi tikumnena uyu.

17 Ndipo zakhala zitafunsidwanso, ndipo apeza ndi mwamuna wolemekezeka pakati pathu . . . (Osati . . . awa posakhala okhawo amuna olemekezeka, tsopano, koma angokhala kuti asankhidwa ndi gulu lotumikira.) M'bale Taylor ochokera ku Henryville, kapena Memphis, ine ndikukhulupirira ndiko ku, Memphis, Indiana. Iye wakhala ali nafe kwa nthawi yina, amachitapo ngati wothandizira ndi chirichonse chimene chikanakhoza kukhala chiri. Kuti mpingo wapeza chifundo ndi iye, kapena gulu lotumikira ndi m'busa, kuti iye avomereze u—udindo waukulu wa kukhala dikoni wa Kachisi tikumnena uyu.

18 Ndipo izo zakhalanso zitafunsidwapo kuti, mkamwini wa M'bale Mike Egan, M'bale—M'bale Bob Harnard, wasankhidwa ndi gulu lotumikira ndiponso ndi abusa, kuti alandire udindo monga msungichuma wa Kachisi tikumukamba uyu, yomwe ili ntchito yolemekezeka, ndipo iyo imasowa chilungamo ndi ulemu.

19 Pa kuchita izi, ine ndikuganiza, abale anga, kuti kukuitanani inu kuchokera pano, kuti uwo ukanakhala ulemu waukulu kwa inu. Ndipo osati zokhazo, koma chinachake choti muzichita.

20 Pa nthawi ino ine ndati M'bale Neville, wothandizana nafe wathu, kuti awerenge zofunikira za dikoni. M'bale Neville, ngati inu mungawerenge izo kuchokera mu Mawu a Mulungu. [M'bale Neville akuwerenga 1 Timoteo 3:8-13—Mkonzi.]:

> *Chomwechonso madikoni azikhala ali olimba, osanena pawiri, osakhala otengeka ndi vinyo kwambiri* ndi *adyera la chisiriro chonyansa;*
>
> *Ogwira chinsinsi cha chikhulupiriro mu chikumbumtima changwiro.*
>
> *Ndipo mulole awa nawonso ayambe ayesedwa; ndiye muwalole iwo kugwira ntchito ya udindo wa udikoni, pokhala atapezeka opanda chowatsutsa.*
>
> *Ngakhalenso akazi awo azikhala olimba, osati onyoza amzawo, olongosoka, okhulupirika mu zinthu zonse.*
>
> *Muzilola madikoni azikhala amuna a mkazi mmodzi, olamulira bwino ana awo ndi apa nyumba pawo.*
>
> *Pakuti iwo omwe atumikira bwino udindo wa udikoni amadziguliranso kwa iwoeni mbiri yabwino, ndi kulimbika kwakukulu mu chikhulupiriro chomwe chiri mwa Khristu Yesu.*

21 Ameni. Ine ndikuti pa nthawi ino ndiwafunse abale awa omwe atchulidwa, ngati iwo angati angoyenda kubwera patsogolo pano ku nsanja kwa mphindi yokha. Ndipo pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa mphindi yokha ya pemphero, ine ndikufuna iwo. . . . Ndipo mpingo ukudziwa chomwe ichi chiri, kuti uku ndi kusankha kwa gulu lanu la madikoni ndi msungichuma wanu.

22 Ambuye Yesu, ndi mwa maganizo abwino, aumulungu kuti ife tikubwera kwa Inu tsopano. Ife tikubwera mwa kulemekeza kwa Mawu Anu Oyera Kwambiri, ife tikubwera tikukhulupirira kuti "Mulole mawu a munthu aliyense akhale olakwika, koma a Mulungu akhale owona." Ndipo ife ndife oyamikira kwa Inu chifukwa cha Mpingo uno umene Yesu waugula ndi Magazi Ake Omwe ofunikira, ndipo watipatsa ife nyumba ino kuti tizipembedzeramo.

23 Ndipo monga oyang'anira zonse a gulu lalikulu ili, lomwe Mzimu Woyera watidzoza ife kuti tikhale, ife tikuyesera tsopano kuti tipereke kwa osonkhana awa gulu la amuna odzipereka, olungama omwe ife tikukhulupirira kuti ndi odzazidwa-Mzimu ndi okonzekera udindowo. Monga izo zanenedwa kale pokhudza gulu la dikoni, "Pitani mukadzifunire pakati panu, amuna a mbiri zabwino ndi wokhala nao Mzimu Woyera, kuti iwo akhoze kumatumikira kwa mchitidwe uwu, kuti azisamalira akazi amasiye ndi ana amasiye, kuti azigawa ndalama, ndi kumasamalira zaubwino wa mpingo." Zaka zamtsogolo, ife tangowerenga kumene zolemba za Paulo Woyera, wamkuluyo, wodzozedwa, yemwe anakhazikitsa kulongosola kwa Malemba pa zofunikira za udindo woterowo.

24 Mulungu, lemekezani amuna awa. Ndipo tsopano uku ndi kusankha, Ambuye, monga mpingo woyima pawokha, monga thupi la Ambuye Yesu, kuti iwo azichita kusankhako. Ndipo [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]. . . ndipo mutsogolere gawo ili la utumiki mwa njira yapadera, mu Dzina lolungama ndi loyera ilo la Yesu.

25 Tsopano ndi mitu yathu itaweramitsidwa, osati mitu yathu yokha komanso mitima yathu, ndipo pamene membala aliyense wa mpingo uno. . . omwe mumabwera kuno nthawizonse ndipo mumawuthandizira iwo ndi chakhumi ndi zopereka zanu, omwe mukuwerengedwa ngati membala wa mpingo uno. Pamene, abusa ndi ine, mwandekha, m—mbusa wothandizira (M'bale Neville) ndi ine tikuyang'anirapo. Ine ndikufunsa ngati mpingo uno wamupeza M'bale Taylor kuti ndi mwamuna wolungama ndi woyenera, mwa kupambana kwa kuganiza kwanu, kuti akhale dikoni pa gulu ili la anthu? Inu musonyeza chomwecho pa kukweza dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Chabwino. Tsopano ngati pali kusiyana kulikonse, inu mungakweze dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Zikomo inu.

26 Kodi aliyense wa mamembala awa a mpingo uno muno amupeza. . . ndi onse, kodi inu mwapeza M'bale Hollin Hickerson kuti ndi mwamuna wolungama ndi wolemekezeka, ndi mwamuna yemwe wapezeka mmaso mwanu kuti ndi woyenera kuti akhale dikoni wa mpingo tikuunena uno? Kodi inu mungasonyeze pa kukweza dzanja lanu lamanja. [M'bale

Branham ayimikira—Mkonzi.] Ngati izo ziri mosiyana, ndiye kwezani dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.]

27 Kodi osonkhana awa amupeza M'bale Collins kuti ali chimodzimodzi, mwamuna wolungama ndi wolemekezeka, ndi woyenera ku ntchito ya kukhala dikoni wa mpingo uno? Inu mungakweze dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Chabwino. Mosiyana, inu mungakweze dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.]

28 Kodi osonkhana awa ampeza M'bale Tony Zable kuti ndi munthu wolemekezeka ndi woyenera pa udindo uwu, wa kukhala dikoni pa gulu ili mu mpingo tikuunena uno? Inu mungakweze dzanja lanu lamanja. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Mosiyana, inu mungakweze dzanja lanu. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.]

29 Kodi osonkhana inu mukumverera kuti M'bale Harnard ndi mwamuna woyenera ndi wolungama, yemwe wakhala ali nafe kwa nthawi ndithu, kuti akhale msungichuma, mlembi—msungichuma wa mpingo uno, kuti azigwira chuma chake ndi kulipira ngongole zake? Ngati ziri choncho, kwezani dzanja lanu lamanja. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Pakakhala pali kusiyana kulikonse, kwezani dzanja lanu lamanja. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.]

30 Ine ndikukhumba kuti ndinene kwa a—abale omwe ayima pa nthawi inoyi, pa phazi la mtanda uwu, kuti mpingo uno, ndi zana pa zana (popanda wosagwirizana nazo konse), wapeza inu nonse oyenera pamaso pa Mulungu ku udindo uwu umene Mulungu wakuitanani inu.

31 Tsopano, inu munati, "Mulole awa ayambe ayesedwa, ndi kuwona ngati iwo akuwukhumba udindo uwu." Mkati mwa masabata angapo, Mulungu akalola, ine ndidzabwerera kuno kuti ndidzasanjike manja pa gulu ili la amuna, kuti tiwapange iwo matra . . . ovomerezeka kapena madikoni a mpingo uno, ndi msungichuma.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha.

32 Ambuye, ife ndife okondwa usikuuno kuti akadalipo amuna omwe akukhala pa dziko lapansi amene angakhoze kumayenda mwaumulungu pamaso pa dziko; mwaumulungu chotero kuti Kachisi, wokhala ndi malamulo okhwima onga omwe uyu ali nawo, akhoza kuvotera anthu asanu mu udindo ngati atsogoleri awo, popanda voti imodzi yotsutsa. Ndife okondwa chifukwa cha iwo, ndipo ife tikumverera kuti Inu munali nafe popanga malingaliro awa, gulu lotumikira ndi ife azibusa.

33 Mulungu, adalitseni amuna awa. Ndipo mulole iwo atumikire udindo uwu ndi mtima wao wonse, podziwa kuti mwa izo zikuwagulira iwo ulemu waukulu Kumwamba. Tsiku lina pamene Mabuku a Kumwamba adzakhala atatsekedwa, mulole Bukhu la zinthu zakumwamba ndi mu Bukhu lalikulu

la Kumwamba lidzatsegulidwe, mulole maina awo adzakhale zana kwa zana pamaso pa Mulungu ndi Mpulumutsi ndi khamu lonse Lakumwamba, kuti zikhale chimodzimodzi mu Ufumu Wake. Adalitseni iwo, Ambuye, ndipo mulole iwo atumikire udindo uwu mwabwino. Mu Dzina la Yesu ife tikukuthokozani Inu mmalo mwao. Ameni.

34 Ine ndikungofuna kuti ndigwirane nanu chanza, [M'bale Branham akugwirana nawo chanza—Mkonzi.] M'bale Harnard, ndi M'bale Zable, ndi M'bale Collins, M'bale Hickerson, ndi M'bale Taylor. Ndakondwa kwambiri kudziwa kuti ife tayanjana nthawi yonse iyi ndi amuna olemekezeka chotero. Mulungu akudalitseni inu tsopano. Ndipo ife tidzakuonani inu pomwepo, mwamsanga ine ndikapuma pang'ono ndi kubwereranso, ndi kuwona momwe inu mukuwukondera udindo wanu. Chabwino, ndi voti yawo, ine ndikuganiza anali zana pa zana, popanda wotsutsa konse.

35 O, kodi sindinu okondwa kuti inu mukuyanjana ndi anthu lero omwe angakhale moyo pamaso pa Mulungu, mwaumulungu, ndi kumakhala moyo pamaso pa dziko lapano ili mu chikhalidwe icho? Ndi chinthu chodabwitsa.

36 Ndipo ndine wokondwa kwambiri podziwa usikuuno kuti ine ndiri ndi mwayi w—wa kukhala nawo amuna awa ndi mpingo uno kuti ndi abwenzi anga. Ndine wokondwa kwambiri kuti Mulungu wandilola ine kuti ndiyanjane ndi Mpingo Wake konsekonse mu dziko. O, iwo ndi onyozedwa ndi okanidwa ndi onenedwa, ndipo monga ine ndinanena mmawa uwu mu uthenga wanga, mwina opanda matope chabe, momwe dziko likuyang'anira pa iwo, ngati "gulu la otentheka," koma Mulungu amayang'ana pa iwo monga ana Ake. Ndine wokondwa kwambiri pa izo. Mwina iwo sangakhoze kukuuzani inu mailosi ake omwe ali kukafika ku mwezi. Iwo mwina sangakhoze kukuuzani inu dongosolo lonse la zopereka kuwala ndi momwe izo zimagwirira ntchito. Koma pali chinthu chimodzi chimene iwo amachidziwa, iwo amalidziwa ora limene iwo anabadwa kachiwiri. Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha iwo.

37 Ndipo monga fanizo laling'ono limene ine ndinaliphunzira, ndipo ine ndiliyanjanitsa ilo usikuuno ndi asungwana anga awiri aang'ono kuti ndikhale ngati ndazipangitsa izo kubwera kwa ife, kuti ndizipange izo kukhala zenizeni kwa ife, kuti inu mukhoze kumvetsa tanthauzo la izo. Mmawa wina, ndikuwuka pa kama . . . Ine ndiri nawo asungwana awiri aang'ono. Mmodzi wa iwo ndi Rebekah, ndipo mmodzi wa iwo ndi Sarah, ndipo iwo ndi asungwana aang'ono a adadi.

38 Ndipo ine ndiri naye mnyamata wamng'ono, Joseph. Ndipo ine ndinali kuchokera ku Chattanooga, ku msonkhano usiku wina, pamene ine ndinali uko mu msonkhano wokopa wotsiriza uwu. Ndipo ine ndinali mu—galimoto, tikupita limodzi ndi

mwana wanga mwamuna wamkulu, Billy. Mkazi wake ndi Meda anali mu galimoto, ndi atsikanawo. Ndipo pamene ife tinali tikupitirira, palibe wina anali atanena kanthu kwa midadada ingapo ya mu mzinda. Ndipo ine ndinali nditadula zolimba ndithu pa anthu usiku umenewo zokhudza momwe iwo anali kuchitira. Ndipo panalibe wina anali atanena chirichonse. Ndipo Joseph wamng'ono anabwera apo ndipo anadzandigwira ine pa phewa, iye anati, "Adadi, inu munalalikira zedi usikuuno!"

39 Ndipo mmawa uno, pamene ine ndinali kuchokapo ndi kupita uko ku Eighth ndi Tenth Street, k. . .kapena Penn ndi Tenth, kani, palibe yemwe ananena kanthu, mkazanga ndi atsikana awiriwo. Ndipo Joseph wamng'onoyo anadzagwira phewa langa kachiwiri, iye anati, "Adadi, kuja, ine ndithudi ndinakukonda kulalikira kuja mmawa uno," iye anatero.

Ine ndinati, "Chabwino, ine ndiri naye wondichemerera mmodzi, ndiye mwana wanga wamwamuna."

40 Ndipo ku mwambi wathu waung'ono. Ntadzuka mmawa wina, nditakhala mu chipinda, Becky wamng'ono anabwera akuthamanga uko ndipo, titi, iye anakwera pa mwendo wanga ndi kuika nkono wake kuzunguliza pa ine, ndipo iye ndi msungwana wamng'ono wa adadi. Ndipo iye anali kundikumbatira ine. Ndipo Sarah wamng'ono analumpha kuchokera pa kama ndi zovala zogonera zake zazing'ono ndipo akanati, nditi, abwere akuthamanga motsatira. Iye ndi wa maso aang'ono abulauni.

41 Becky wamng'ono ananena kuti, "O, Sarah, palibe chifukwa choti iwe udzere, chifukwa ine ndawatenga adadi onse ndekha. Adadi onse ndi anga!" Ndipo Sarah wamng'ono, milomo yake yaying'ono inagwera pansi, maso ake aang'ono abulauni atawaphimba. Ine ndinalozera monga *chonchi* ndi kutululutsira kunja bondo linalo, ndipo iye anabwera nadzakwera pa ilo.

42 Becky ali ndi miyendo yaitali, kotero iyo inkafika pansi. Sarah wamng'onoyo anali akuphunzira kuyenda, kotero ine ndinayika mikono yonse momuzunguliza Sarah. Sarah wamng'onoyo anayang'ana kwa Becky nati, "Becky, iwe ukhoza kukhala nawo adadi onse, koma adadi anditenga ine yense!"

43 Ndipo ine ndikuganiza umo ndi momwe ziriri pano. Ife tikhoza kusamadziwa fioloje yonse, osadziwanso mawu aakulu onse Achigriki, gulu la anthu ili likhoza kusamadziwa. Koma pali chinthu chimodzi chotsimikizika, ine ndikukhulupirira Yesu ali ndi yense wa *ife*. Ameni.

Chabwino, M'bale Neville.

Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org